

CHIYAMBI

NKHANI YOTCHUKA YOWONEKA NDI KUBWEREZA MWACHIDULE

Kutanthauzira:

Chokhumudwitsa – kulanda nkhongono, chiyembekez, kapena kulimbika mtima, kutaya mtima.

Funso

Kodi inu muli ndi pati pamene muli ndi kuthekera ndi kulimbana ndi zokhumudwitsa?

Chokhumudwitsa ndi nambala 1 chowononga madongosolo a Mulungu a mmiyoyo yathu; tisanalandire chabwino kwambiri ndi chapamwamba kwambiri chochokera kwa Mulungu, amiri a ife timataya kaye kampango.

DONGOSOLO LA MULUNGU LOPHERA CHILOMBO CHA CHOKHUMUDWITSA.

K – Khalidwe

Chifuniro cha Mulungu mmavuto – CHIPILIRO CHA CHIMWEMWE

Muchiyese chimwemwe chokha abale anga amene mukugwa mmayesero a mitundu mitundu; 3 pozindikira kuti chiyesedwe cha chikhulupiriro chanu chichita chipiriro. 4 Koma chipiriro chikhale nayo ntchito yache yangwiro, kuti mukakhale angwiro ndi opanda chirema, osasowa kanthu konse. (Yakobo 1:2-4)

C – Chida

Lonjezo la Mulungu mu dongosolo – NZERU ZOPAMBANA KWAMBIRI

Koma wina wa inu ikamusowa nzeru, apemphe kwa Mulungu, amene apatsa kwa onse modzala manja, niwosatonza; ndipo adzampatsa iye. Koma apemphe ndi chikhulupiriro wosakayika konse; pakuti wokayikayo afanana ndi funde la nyanja lotengeka ndi mphepo ndi kuwinduka nayo. Pakuti asayese munthu uyu kuti

adzalandira kanthu kwa Ambuye; munthu wa mitima iwiri akhala wosinkhasinkha pa njia zache zonse. (Yakobo 1:5-8)

M – Moyo wa UMulungu

Mankhwala a Mulungu a chipiriro – MAONEKEDWE A UMULUNGU

Koma mbale woluluka adzitamandire pa ukulu wache; pakuti adzapita monga duwa la udzu. Pakuti laturuka dzuwa ndi kutentha kwache, ndipo laumitsa udzu; ndipo lathothoka duwa lache, ndi ukoma wa maonekedwe ake waonongeka; koteronso wachuma adzafota mmayendedwe ache. Wodala munthu wakupirira poyesedwa; pakuti pamene wavomerezeka, adzalandira korona wa moyo amene Ambuye adalonjezera iwo akumkonda lye. (Yakobo 1:9-12)

KUYIMABE MOLIMBA MU NTHAWI ZOLIMBA KUMAFUNA IFE:

1. Kupeza maonekedwe a Mulungu mu zinthu zochitika zotizungulira. (Yakobo 1:9-11)
 - Motani? Poyang'ana zinthu zochitika zotizungulira kudzera mmaso mwa CHIKHULUPIRIRO.
2. Kupeza mawonekedwe a Mulungu mu tsogolo lathu. (Yakobo 1:12a)
 - Motani? Poyang'ana tsogolo lathu kudzera mmaso mwa CHIYEMBEKEZO.
3. Kupeza mawonekedwe a Mulungu mu chilimbikitso. (Yakobo 1:12a)
 - • Motani? Poyang'ana pa chilimbikitso chathu kupyolera mmaso a CHIKONDI.

KUMANGIRIRA/KUBWEREZA

MUKHOZA KUPHA CHIROMBO CHA CHOKHUMUDWITSA!

1. Kuwunikiranso zochitika zokuzungulirani.
 - Mayeso: Chikhulupiriro changa chili mu zinthu zakutha kapena mu zinthu ZOKHALITSA?
2. Kuwunikiranso zolunjika zanu.
 - Mayeso: Chiyembekezo changa chotsimikizika ndi muyeso wa mavuto anga kapena ndi chitsimikizo chosasintha cha MALONJEZO a Mulungu?
3. Kuwunikiranso chilimbikitso chanu.
 - • Mayeso: Chilimbikitso choyambirira mumtima mwanga ndi CHIKONDI CHA KHRISTU kapena kungopezako mpumulo ndi kudzisangalatsa ndekha?

MAFUNSO OKAMBIRANA

1. Lembani chiganizo chimodzi chosavuta ndi chomveka bwino cha zimene panopa (kapena zothekera) zikukhumudwitsani.
2. Gawanani ndi ena yankho lanu la funso loyamba ngati muli omasuka kutero ndipo ndi kuyenera kuchita choncho.
3. Kambiranani za mphamvu za mawonedwe pamene zikugwirizana ndi nyengo yanu. Dutsani mufundo zitatu zimene zapangidwa mu Yakobo 1:9-12 ndi kukamba za mmene zawunikira pa zophunthwitsa zenizeni zimene mukukumana nazo.
4. Pemphererani wina wake amene mukumudziwa amene akukumana ndi “dziko losweka.”